EXAMINATION NO: _______________

# KACHULU ZONE EXAMINATION BOARD

2023-2024 ZONAL MOCK EXAMINATION FOR STANDARD 8

# CHICHEWA

(Malikisi 100)

**Subject Number: P032**

**Thursday 14th March, 2024.** **Time Allowed: 2 h 15 min**
**01:00 – 03:15 pm**

**Dzina lanu: ______________________________________________**

**Dzina la Sukulu yanu: ______________________________________**

## GAWO A (malikisi 30)

**Langizo:** Yankhani funso limodzi lokha pamafunso awiri ali m'munsiwa. Sankhani chimangirizo kapena kalata. Mawu a chimangirizo chanu kapena kalata yanu asachepere 100 kapena asapitilire 150.

**1.** Lembani chimangirizo pa mutu uwu**:**

**MASEWERA A KUMUDZI KWATHU**

Mwazina tsatani izi polemba:

**Ndime yoyamba**

- Dzina la masewera omwe amachitika ku mudzi kwathu
- Komwe masewerawo amachitikira
- Nyengo imene masewerawo amachitikira

**Ndime ya chiwiri**

- Zinthu zomwe amagwiritsa ntchito pa masewerawo
- Kufunika kwa masewerawo
- Maguru a anthu amene amachita masewerawo

**Ndime ya chitatu**

- Zomwe anthu a kumudzi kwanu akuchita kuti masewerawo asaiwalike. (malikisi 30)

**KAPENA**

**2.** Lembani kalata kwa a malume anu yofotokoza za amayi awo amene adadwala Malungo masiku apitawo

Mwazina tsatani izi polemba:

**Ndime yoyamba**

- Cholinga cha kalata
- Tsiku lomwe matendawo adayamba
- Momwe matendawo adayambira

**Ndime ya chiwiri**

- Chithandizo chomwe wodwalayo adalandira
- Zomwe mukufuna kuti a malume anu achite

Ndime ya chitatu

- Malangizo amene mudapeleka kwa amayiwo pofuna kupewa matenda a malungo

________________________________________
________________________________________
________________________________________
________________________________________
________________________________________
________________________________________
________________________________________
________________________________________

**GAWO B** (malikisi 20)

**KUMVETSA NKHANI**

3. Werengengani nkhani yotsatilayi mosamala kwambiri kenako yankhani mafunso otsatilawa

Mudzi wa mfumu Masasa udali kuzambwe kwa m'dera la mfumu yayikulu Sunganani. Mudziwu udatchuka kwambiri chifukwa cha umodzi ndi Khama la mbadwa za m'mudzimo. Anthu a mudzimo amagwira ntchito zachitukuko modzipeleka ndipo adadzimangira midadada ya Sukulu, Chipatala, Positi Ofesi ndi Msika waukulu. Iwo adakumbaso zitsime, adalambulaso misewu ndi kumanga maulalo. Mudziwo udali ngati katawuni ka kumudzi.
Makhumutcha ambiri ochoka ku maiko adayambitsa ntchito za malonda m'mudziwo. Achinyamata ambiri adapeza zintchito zolembedwa. Ngakhale ena amapeza zintchito motero mfumu Masasa sidali yokondwa kweni kweni. Iyo idali yodandaula chifukwa anthu antchito zamalonda ndiwo amalemera.
Mfumu Masasa idaitanitsa nduna zake kut akambilane njira zothandizira anthu a m'mudzi mwawo kuti nawoso adzipeza ndalama.
Mfumu Masasa idaitanitsa msonkhano wa anthu ake ndi cholinga chowafotokozera masomphenya ake. Msonkhanowo udachitikira pa malo pomwe imazengelapo milandu. Bwalolo limadziwika ndi dzina la kuti Kachere. Chifukwa cha chimtengo cha Kachere chomwe chidali pa bwalopo.
Mtumiki wa mfumu ndiye amene adamemeza za Msonkhanowo loweluka usiku. Iye adamemeza kuti aliyese akapezeke ku Kachere tsiku lotsatilaro nthawi ya kumasana.

M'mene dzuwa limaswa mtengo niliti akalambula bwalo atayamba kale kusonkhana. Awa anali Ana apakati pa zaka zisanu ndi ziwiri ndi khumi. Dzuwa litapendeka Fumbi la anthu ndi madoda lidakhamukukila ku Kachere. Posakhalisa mfumu idatulikira ndi nduna zake zitatu. Ndunazi zidali a Gopani, a Sags ndi Chiutula.
Pa msonkhanowo mfumu inalimbikitsa achikumbe a mudzi mwake kutazipanga maguru kut azigulisa mbewu zawo pamodzi. Mudziwu udatchuka kwambiri ndipo mfumu Musasa idamveka posepose mfumu yayikulu Sunganani.
(Buku la ophuzira la sitandade 7)



Continued//…….

Tsopano yankhani mafunso otsatirawa pa mizere ili pansi pa funso lililonse.

a. Kodi mudzi wa Musasa udali m'dera liti?
…………………………………………………………………………….…………………. (malikisi 1)

b. Tchulani zizindikiro ziwiri zokha zomwe zidabwera m'derali
i. ……………………………………………………………………………………………….
ii. ……………………………………………………………………………………………. (malikisi 2)

c. Nchifukwa chiyani mfumu masasa idaitanisa msomkhano wa anthu ake m'derali?............................................................................................................................ (malikisi 2)

d. Nchifukwa chiyani bwalo la mfumu limadziwika ndi dzina loti Kachere
………………………………………………………………………………………………..

e. Perekani matanthauzo a mawu awa:
   i. Khumutcha……………………………………………………………………..….
   ii. Fumbi la anthu………………………………………………………………….…… (malikisi 2)

f. Pezani mawu mnkhaniyi omwe mawu otsutsana ake ndi awa:
   i. Kumvuma……………………………………………………………………….…
   ii. Ulesi…………………………………………………………….................................. (malikisi 2)

g. Perekani mayina awiri anduna za mfumu Masasa
   i. ………………………………………………………………………………..……….
   ii. ……………………………………………………………………..……………. (malikisi 2)

h. Anthu anadziwika bwanji kut mawa kuli msonkhano
............................................................................................................................. (malikisi 1)

i. Kodi anthu amudzimo adachita chiyani atamva za uthenga wa msonkhano?
……………………………………………………………………….……………………. (malikisi 2)

j. Lembani mawu ofanana ndi mawu oti:
a. Zengamilandu ……………………………………………………………….……. (malikisi 1)

k. Fotokozani ubwino wolimbikira ntchito
………………………………………………………………………………………………... (malikisi 2)

l. Perekani mutu wa nkhaniyi …………………………………………….………………… (malikisi 1)

**GAWO C** (malikisi 10)

Yankhani mamfuso onse awiri m'gawoli

**4.** Werengani kankhanika ndipo muyankhe mafunso otsatilawa.

Dzimbiri: Zikomo! Zikomo! Zikomo kuno!
Nanthochi: Ee! Alowe. Monitu, nanga muli bwanji?
Dzimbiri: Ine ndili bwino, sindidziwa inu muli bwanji? Ndangomva kuti atsibweni si moyo!

**MAFUNSO**

I. Ndi malonje anji akupelekedwa mnkhaniyi?
.............................................................................................................. (malikisi 1)

II. Kodi Nanthochi ndi ndani wake wa Dzimbiri
…………………………………………………………………………….. (malikisi 1)

III. Kodi mawu akuti "si moyo" akutanthauzanji?
……………………………………………………………………….…. (malikisi 1)

b) Lembani mfundo imodzi momwe mungasamire wodwala.
……………………………………………………………………………..…. (malikisi 1)



Continued//…….

c) Perekani kufunika kumodzi kwa nyama zakutchire

…………..……………………………………………………………………….…… (malikisi 1)

**5. Kupanga ziganizo**

Panganizo ziganizo zomveka bwino ndi mawu awa:

1) Sina
…………………………………………………………………………….. (malikisi 1)
2) Zizwa
…………………………………………………………………………….. (malikisi 1)
3) Wa ulesi
…………………………………………………………………………….. (malikisi 1)
4) Du
…………………………………………………………………………….. (malikisi 1)
5) Ganizo
…………………………………………………………………………….. (malikisi 1)

GAWO D (malikisi 40)

Zungulizani lembo (A, B, C kapena D) m'mafunso otsatilawa:

**Mafunso 6 mpakana 10**: Sankhani mitundu ya mawu omwe atsekedwa mzere kunsi kwawo mziganizo zotsatirazi.

**6.** Zonse **zoyera** ndi zanga.
  a. Mperekezi
  b. Mfotokozi
  c. M'neni
  d. Mlumikizi

**7.** Kambuku **ndi** chilombo choopsa.
  a. Mlumikizi
  b. Mvekero
  c. Mperekezi
  d. M'neni

**8.** Gulu lija **lakhaulitsidwa** zedi.
  a. Muonjezi
  b. Mlumikizi
  c. M'neni
  d. Mfotokozi

**9.** **Ife** tizithokoza nthawi Zonse mukatithandiza.
  a. Muonjezi
  b. Mlowam'malo
  c. M'neni
  d. Dzina

**10.** Ana **ndi** aphuzitsi akukambirana
  a. M'neni
  b. Mperekezi
  c. Mvekero
  d. Mlumikizi

**Mafunso 11 mpakana 13:** Sankhani maguru a mayina omwe atsekedwa mzere kunsi kwawo.

**11.** Mkango ndi nyama yolusa.
  a. Li-, Ma-
  b. Mu-, A-
  c. Mu-, Mi-
  d. Chi-, Zi-

**12.** Mavuto ndi Lute akulimbirana chivululu.
  a. Chi-, Zi-
  b. Ka-, Ti-
  c. I-, Zi-
  d. U-, Zi-

**13.** Phungu wadera lino ndi wachitukuko.
  a. LI-, Ma-
  b. Chi-, Zi-
  c. MU-, Ai-
  d. U-, Ma-

**Mafunso 14 mpakana 16**: Sankhani mayina omwe ali ndi m'mitundu yotsatilayi.

**14.** Dzina lopanda mwinimwini
  a. Ulesi
  b. Mulu
  c. Shire
  d. Nyakwawa

**15.** Dzina la mwinimwini
  a. Mtungo
  b. Bambo
  c. Zomba
  d. Sukulu

**16.** Dzina la unyinji
  a. Uve
  b. Phava



Continued//…….

c. Anyamata
d. Malingaliro

**Mafunso 17 ndi 19:** Sankhani chaching'ono cha mawu omwe atsekedwa mzere kunsi kwawo.

**17.** Lero tidyera **<u>mpiru</u>** wotendera.
a. Mbande
b. Masamba
c. Buthu
d. Njere

**18.** Alinafe ndi **<u>mtsikana</u>** wokongola.
a. M'nyamata
b. Ndoda
c. Buthu
d. Mbewa

**19.** Ndibwino kumaweta **<u>Nkhuku</u>** zachizungu.
a. Chipsolopsolo
b. Kasawala
c. Mlumbwana
d. Anapiye

**Mafunso 20 mpaka 22:** Sankhani ntchito za "ndi" m'zinganizo zomwe zili m'musizimu.

**20.** Abambo, amayi **<u>ndi</u>** ana akulima.
a. Kukhala mlumikizi
b. M'neni
c. Mlowam'malo
d. Mvekero

**21.** Mateyu, uzilankhula mfundo za **<u>ndi</u>** ngati ndiwe mwamuna.
a. Mfuwu
b. Mperekezi
c. Mvekero
d. M'neni

**22.** Zione ali **<u>ndi</u>** khalidwe la bwino.
a. Mperekezi
b. Mlumikizi
c. Mfuwu
d. Mlowam'malo

**Mafunso 23 mpaka 25:** Sankhani matanthauzo oyenera azining'a zotsatirazi.

**23.** Kuyenda utsi uli tsitu.
a. Kupusa
b. Kunsiza
c. Kuyenda utatsizina
d. Kuyenda mofatsa

**24.** Waziwala m'maso.
a. Wopupuluma
b. Wolalata
c. Wopenga
d. Wosokonezeka

**25.** Meta nkhanga mpala.
a. Kuvulala
b. Kumeta mpala
c. Kumeta tsumba
d. Kukhaulitsa

**Mafunso 26 mpaka 28:** Sankhani mitundu ya alumikizi omwe atsekedwa mzere kunsi kwawo

**26.** Ndipita nanu **<u>ngakhale</u>** m`thupi mukuphwanya.
a. Wamgwirizano
b. Wopatula
c. Wophatikiza
d. Wa umyinji

**27.** Mundibweretsere mfutso **<u>osati</u>** mazira.
a. Wamgwirizano
b. Wophatikiza
c. Wamaonekedwe
d. Wopatula

**28.** Udzu **<u>ndi</u>** mitengo zili mgulu la mitengo.
a. Wopeneka
b. Woluzanitsa
c. Wopatula
d. Waubale

**Mafunso 29 mpaka 32:** Sankhani chiganizo chimene chili ndi zizindikiro zoyenera za m`kalembedwe m`ziganizo zotsatirazi.

**29.** :
a. Yohane amaweta nkhuku, nkhumba, ndi mbira
b. Yohane amaweta, nkhuku, nkhumba ndi mbira.
c. Yohane amaweta nkhuku, nkhumba ndi, mbira.
d. Yohane amaweta nkhuku, nkhumba ndi mbira.

**30.** :
a. Anafika kunja kuli mbee!
b. Anafika, kunja kuli mbee.
c. Anafika kunja kuli mbee?
d. Anafika kunja kuli mbee.

**31.** :
a. Maria amayenda, monyada.
b. Maria: amayenda, monyada.
c. Maria amayenda monyada.
d. Maria; amayenda monyada.

**32.** :



Continued//…….

a. Kodi ndiwe yani?
b. Kodi ndiwe yani.
c. Kodi ndiwe yani
d. Kodi ndiwe “yani?

**Mafunso 33 mpaka 35:** Sankhani mitundu ya nthambi za ziganizo zosaima pazokha zomwe zatsekedwa mzere kunsi kwawo m`ziganizo zotsatirazi.

**33.** Mvula ivuta kubwera **chifukwa tadula mitengo yonse.**
a. Ya dzina
b. Yamfotokozi
c. Yoyima payokha
d. Ya muonjezi

**34.** Bamboo **amene akubwera apoyo** ndi amalume anga.
a. Yoyima payokha
b. Ya dzina
c. Ya mfotokozi
d. Ya muonjezi

**35.** **Kuti Nyengo yasinthiratu** sinkhani yobisikanso.
a. Ya dzina
b. Ya muonjezi
c. Ya mfotokozi
d. Yoyima payokha

**Mafunso 36 mpaka 38:** Sankhani mikuluwiko yomwe ikutsutsana m`matanthauzo ndi yotsatirayi.

**36.** Zengerezu adalinda kwanu kwanu.
a. Njuchi zikachuluka siziika uchi
b. Tsabola wakale sawawa
c. Mwana wamwini ndi gaga saundika
d. Kuona maso a nkhono n`kudekha

**37.** Ukayendera m`tchire wayendera zonse.
a. Ukayendera nzengo usamati asakhwi afumbula
b. Walira mvula walira matope
c. Ali dere n`kulinga utayenda naye
d. Likaomba otheratu

**38.** Mawu aakulu akoma akagonera.
a. Lende n`kukankhana
b. Tsabola wakale sawawa
c. Walira mvula walira matope
d. Akulu akulu ndi mdambo mozimira moto

**Mafunso 39 mpaka 41:** Sankhani misintho ya aneni imene yatsekedwa mizere kunsi kwawo.

**39.** Mwana **wamenyedwa** ndi wakuba.
a. Wochititsa
b. Wochitidwa
c. Wochititsitsa
d. Wom`chitira

**40.** Magule ambiri aku Malawi **amavinika.**
a. Wotsutsa
b. Wam`chibisira
c. Wonyanzitsa
d. Wochitika

**41.** Kalatayi ndinamata; **wamatura** ndani?
a. Wotsutsa
b. Wochitidwa poyera
c. Wochititsitsa
d. Wochitirana

**Mafunso 42 mpaka 45:** Sankhani mawu ofanana m`matanthauzo ndi omwe atsekedwa mzere kunsi kwaziganizo zili m`musimu.

**42.** Ambewe amaweta **mberere** zambiri.
a. Ngondolo
b. Thadzi
c. Mbewa
d. Tonkhwe tonkhwe

**43.** Nkhuku zonse zidafa ndi **chitopa.**
a. Chigodola
b. Khunyu
c. Chipumphu
d. Gomo

**44.** **Nkhalamo** ndi nyama yolusa kwambiri.
a. Pumbwa
b. Kasontho
c. Malingwere
d. Mkango

**45.** A Nasani ndi **namfedwa.**
a. Mfumukazi
b. Mpongozi
c. Mferekazi
d. Mvuwu

**MAFUNSO ATHERA APA**



Continued//…….